# MOMWE
# CHIKHRISTU
# CHINAYAMBIDWIRA
# NDI KUNYENGA ANTHU OCHULUKA

## KALENDALA YA PANGANO LA YAHUWAH

*Kugawa Moyenera Mawu a Choonadi*

Poyamba tikufuna kufotokoza kuti Phunziroli sinalinganizidwe ndicholinga chofuna kudzudzula kapena kuweruza aliyense, koma kulimbikitsa anthu kuti azichita kafukufuku komanso aziphunzira okha ndikupeza ngati zinthu zomwe akhala akuziphunzira /kuphunzitsa ndi kuzikhulupirira kwa nthawi yayitali zili molingana ndi Malemba opatulika a Mlengi wamphamvu zonse ***Yahuwah.***

***Izi ndizimene anthu a ku Bereya ankachita, ndipo tikulangizidwanso kutsatira chitsanzo chawo!***

Molingana ndi***1Atesalonika 5: 21***,“***Yesani zinthu zonse, gwiritsitsani chokomacho.” KJV***

***CHONDE DZIWANI IZI KUTI MUSASOKONEZEDWE***:

Timagwiritsa ntchito mayina eni eni aMlengi wathu ndi mwana wake.

Timatchula mlengi wathu amene analenga kumwamba ndi dziko lapansi ndi zinthu zonse kuti **Yahuwah** limeneli ndilo dzina lake lenileni la atate-wathu wakumwamba . Dzina la mwana wake ndi **Yahusha** osati ***Yesu.*** Iye ndiye Mwana wobadwa yekha wa (YHVH) Yahuwah atate.

Mau oti Elohim (Mulungu) amatanthauza Wamphamvu kapena Wamphamvuzonse. Uwu ndi ulaliki wozama komanso

wofunikira kwambiri ndipo uyenera kumvesetsedwa bwino kwambiri, makamaka kwa ozitcha Akhristu odzipereka.

Komabe, tiyeni tikambirane pamodzi ndi kukhala ndi maganizo omasuka. Ngakhale kuti Choonadi chimapweteka koma chimachiritsanso; bodza limakoma koma limapha. Osavomereza mawu athu okha kapena mawu a anthu omwe anasokhanitsa phunziroli kapena azineneri angoti mbweewa ndi azibusa omwe amatitumikira.

***Chitani kafukufuku wanu, popeza pali zambiri pamutuwu, zomwe zitsegule maso aaliyense amene ali ndi chidwi chofuna kudziwa chowonadi.***

Anthu miyandamiyanda ananyengedwa kale pankhani yachipembedzo ndipo masiku ano akupusitsidwabe. Nkofunika kuti tisanyengedwe, chifukwa tili ndi Kumwamba komwe tingapeze komanso gehena yoti tipewe.

Ino ndi nthawi yoti tipeze  chowonadi ndi kusankha njira yoti titenge, kaya ndi njira yopita ku chipulumutso kapena ku chiwonongeko.

Malemba amene agwiritsidwa ntchito muphunziro lino amachokera mu baibulo lotchedwa “The Scripture Translation” mchingerezi

***Kumbukirani*** kuti: *"Sitilimbana ndi mwazi ndi thupi, koma ndi maukulu, ndi maulamuliro, ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi a mdima wa pansi pano, ndi zinthu zauzimu za choipa m'zakumwamba."* (***Aefeso 6:12***)

M'pofunika kutsindika mfundo yakuti Satana ndi amene amachititsa chinyengo chonsecho!

***Kodi mawu akuti chikunja amatanthauza chiyani?***

Mawu akuti chikunja amatanthauza wosakhulupirira, munthu amene amapembedza mafano m'mawonekedwe monga matabwa, mwala kapena chifaniziro chimene chaletsedwa m'Baibulo.

## ***CHIKHRISTU***


***Kodi mukudziwa kuti kunali akhristu amene amapembedza mafano mzaka mazana ambuyomo Yahusha Mesiya asanabwere kudzatibadwira pansi pano?***

Constantine ndi Arius Constantine Wa Chigiriki (Constantine wamphamvu) Mfumu ya Roma kuyambira 306 mpaka 337, amadziwika kuti anali mfumu yoyamba ya Roma kutembenukira ku Chikhristu chomwe ndichodabwitsa kwambiri, Arius waku Libya (256-356 A.D.) wobadwa kuchokera ku Africa zaka mazana angapo pambuyo pa Ptolemy 1, anali ndi vuto ndi ufumu wa Roma kuphunzitsa

anthu aku Afirika komanso  anthu a Chiroma kulambira fano ndi kukondwerera imfa.

Anali kuonedwa ngati wampatuko, wodzinenera kukhala wokhulupirira (wa Mulungu), amene amasunga malingaliro achipembedzo mosagwirizana ndi kuvomerezedwa ndi mpingo wake (zimene akuluakulu achipembedzo olamulidwa ndi boma kaŵirikaŵiri amaziwona kukhala choonadi).

Bungwe la Nicea - Bungwe lomwe linalenga ***Yesu Khristu***.






Serapis Christus Greco Wachiroma, cha m'ma ***135 B.C.E***. Chithunzi cha nsangalabwi mu London (Briteni) musiamu ndi chithunzi chomwe amagwiritsa ntchito Monga Khristu (Yesu) lero. Christus analinso ndi  dzina lotchedwa kuti Serapis.

**Serapis anali ndani? (Chiyambi cha YESU KHRISTU)**

Mulungu wopangidwa ndi Graeco-mulungu wa ku Aiguputo yemwe adapangidwa m'zaka za ***300 B.C***.,wowonetsedwa ngati wachi Giriki, koma wokhala ndi zida za Aigupto, zomwe zinkayimira chuma ndi chiukitso.

Chifukwa chakuti anayamba kukopa otsatira achiroma ambiri chifukwa cha ziphunzitso zake zimene zinali zosemphana ndi Aroma, Constantine anaitanitsa msonkhano wa mabishopu onse kuti anyoze Arius. ***Bungwe la ku Nicaea***.

Pa nthawi yomwe msonkhanowu unalikuitanidwa, panalibe kutchulidwa konse kwa dzina loti Yesu Khristu; palibe munthu amene anakhalapo ndi dzina lakuti YESU Kristu, ndipo mfundo yofunika ndi yakuti zonsezi zinachitika ***Anno Domino (A.D.)*** (zimene Akristu amati amatanthauza pambuyo pa imfa ya Kristu) m'Chilatini amatanthauza ***'m'chaka cha ambuye'***. Dzina lakuti Yesu Khristu kunalibe msonkhano usanaitanidwe (werengani mawu onenedwa panthawiyo).

Zitatha izi mpamene anapereka kwa anthu dzina lakuti ***YESU KHRISTU***. Kodi iwo ankanena za Ambuye?Nanga m'mbuyomo ankaitanila ndani?

Mafumu a nthawi imeneyo amatchedwa ambuye kapena Milungu. Ngati Mesiya kunalibe panthawi yomwe

msonkhanowu unkachitika kapena kumva za iye, kodi akulambira ndani masiku ano?

Serapis Christus?

**Mndandanda wa Ziphunzitso Zambiri Zachikunja Zomwe Zimaphunzitsidwa mu Chikhristu sizipezeka m'Baibulo**.

**1** *Tsiku la Sabata lomwe ndi tsiku lachisanu ndi chiwiri linasinthidwa kukhala la Sande lomwe ndi tsiku loyamba pa mlungu, polemekeza Kulambira Dzuwa (Baala/ Lord)*.

Palibe vesi limodzi la m'Baibulo lothandizira kupembedza kwa dzuwa (Sande) tsiku loyamba .Sabata( tsiku lachisanu ndi chiwiri) ndi ***"chizindikiro***" chomwe mumawonetsa muli padziko lapansi pano kubwerera kwa Mlengi kuti mukumudziwa. Ndi chikondwerero cha Dongosolo la Chipulumutso chomwe chanavumbulutsidwa ngati masiku 6 ***(kuimila zaka zikwi zisanu ndi chimodzi( 6000)*** pomwe timagwira ntchito pansi pa themberero la Adamu (tiyenera kugwira ntchito kuti tipeze moyo), kenako zaka ***chikwi (1000)*** zakupumula ku temberero limenelo. Ngati simusunga masabata ake, ndiye kuti simudziwa Mlengi, ndipo sindinu mwana wake.

**2**. ***Masiku amapwando asanu ndi awiri 7 a Yahuwah adalowedwa m'malo ndi Matchuti / mipumulo yachikunja***

***kuphatikizapo Khrisimasi, Pasaka, Tsiku la Valentine, Tsiku lakuthokoza, Halloween, Tsiku la Abambo ndi Tsiku la Amayi. Palibe lililonse la zimenezi limene limapezeka m'Baibulo ndipo matchuti/mipumulo yonse imeneyi imachokera ku zikhulupiriro zachikunja za ku Babulo. Yahuwah amadana ndi mapwando achikunja amenewa.***

Khrisimasi, Mitengo ya Khrisimasi zonse ndizachikunja zolimbikitsidwa ndi Chikhristu Dzina lenileni kapena kuti chizindikiro chenicheni cha "***Santa Clause"*** ndi Nimrod mwiniwake ndipo Mtengo wa khrisimas ndi chikumbutso kwa iye.

Tikuwona Nimrodi ali ndi ndevu zazitali zoyera zomwe zikujambulidwa bwino, "Mtengo wa Khrisimasi" komanso mphalapala kumayambiriro kwa 2000 BC, inde zaka 2000 BC "Chikhristu" chisanalengedwe: ***Tsiku Lobadwa la Nimrodi ndi Tamuzi ndi Kubadwanso kwa Dzuwa. (Khrisimasi***)

`Chiyambi cha Khirisimasi chakhala ndipo chikupitiriza kuwululidwa kaamba ka chiyambi chake chenicheni: "Nimrode anayambitsa mpatuko waukulu wadziko wolinganizidwa ndi Mulungu amene akulamulira dziko lino kufikira tsopano. Nimrodi anakwatira amayi ake, amene dzina lawo linali Semiramis. Mkazi wake,wotchēdwa Semiramis, anafalitsa chiphunzitso choipa cha kupulumuka kwa Nimrodi monga

munthu wauzimu. Patsiku lililonse lakubadwa kwake, iye ananena kuti, Nimrode ankachezera pa mtengo wobiriwira nthawi zonse n'kusiyapo mphatso. ***December 25*** linali tsiku la kubadwa kwa Nimrodi. Ichi chinali chiyambi chenicheni cha ***Mtengo wa Khrisimasi*** .

Khrisimasi pokhala kubadwa kwa"***Yesu"*** zinachokera ku Chipembedzo Chachinsinsi cha Babulo. Pofuna kuti atetezere ulamuliro wake monga Mfumukazi ya Babulo pambuyo pa imfa ya Nimrodi, Semiramis anayenera kupanga njira yosunga "Mzimu wa Nimrodi" wamoyo. Iye anali atatchuka kale monga Baala (mulungu wa dzuwa) ,choncho ankafunikira kuti abwerenso kwa anthu. Semiramis adafunsana ndi okhulupirira nyenyezi omwe adamuuza kuti dzuwa ***"limafa" pa December 21*** (tsiku lalifupi kwambiri la m'chaka) koma kenako limayamba kukhalanso ndi moyo madzulo a ***December 24*** pamene masiku ayamba kukula.

***<u>Kodi "Khirisimasi" inaperekedwa motani kwa ife mu "Chikristu"?</u>***

Mu nthawi ya Romu wa chikunja,Yahusha atapachikidwa,ndi pamene , iwo anayambitsa "***Saturnalia***" polemekeza mulungu ***Saturn***. Chinali chikondwerero chosayeruzika chomwe chinachitika pa ***December 25***, tsiku lobadwa Nimrodi ndi

Tamuzi mwana wake. Chaka chilichonse, munthu osalakwa ankasankhidwa ndi anthu kuti aziperekedwa nsembe kwa milungu yawo. Munthuyo amakakamizidwa kuchita nawo mitundu yonse ya zosangalatsa zakuthupi (kudya, kugonana, ndi zina) sabata yonse yopita ku Saturnalia, kenako kuphedwa pa ***Disembala 25*** ndi cholinga chopeza madalitso a milungu chaka cha zokolola zikubwerazo.

Kuwonjezera pa nsembe za anthu, kunali kuledzera kofala kwambiri ndipo anthu ankapita nyumba ndi nyumba kuyimba nyimbo. ***Anthu amatsanzira nsembe za anthu podya mabisiketi ooneka ngati anthu (timawatcha amuna a Jinja buledi). The Encyclopedia Britannica voliyumu 24 tsamba. 231 amatiuza ife kuti anthu ankapatsana mphatso. Makamaka kwa ana m'mawonekedwe a "zidole" zomwe zimayimira anthu operekedwa nsembe kwa milungu yopanda chilema.***

Chikhristu chinaphatikiza Saturnalia m'chipembedzo cha Constantine (Chikhristu) akuchitcha Khirisimasi m'zaka za m'ma ***400 AD.*** Palibe chikondwerero choterocho m'Baibulo. Chidachokera mwachindunji ku Babulo.

***<u>Chiyambi cha Mtengo wa Khrisimasi Wachikunja</u>***

***Yahuwah amatiuza ife kuti tisaphunzire njira za amitundu mu Yeremiyahu 10:2-4*** "Musaphunzire njira ya amitundu, ndipo musawopsedwe ndi zizindikiro zakumwamba; (wokhulupirira nyenyezi) chifukwa amitundu achita mantha nazo…Pakuti miyambo ya anthu ndi yachabechabe: pakuti munthu atema mtengo m'nkhalango, ntchito ya manja a mmisiri ndi nkhwangwa. Amaukongoletsa ndi siliva ndi golidi; amachikhomera ndi misomali ndi nyundo kuti lisagwedezeke. Liwu lachihebri lotanthauza "nkhalango" pankhaniyi ndi – 'asherah אֲשֵׁרָה '




.

Ashera: zifanizo (zopembedza mafano); ***<u>Wachibabulo</u>*** (Astarte/Ishtar) - mulungu wamkazi wa kukanani (wamwayi ndi wachimwemwe), wolingaliridwa kukhala mkazi wa Baala

wotchedwa Ishtar, mafano ake; mulungu wamkazi, milungu yaikazi; zithunzi zake; mitengo yopatulika kapena mizati yoikidwa pafupi ndi guwa la nsembe. **Chiyambi cha Mtengo wa khrisimas (X kapena "mtanda" ndi chizindikiro cha Tamuzi) kwenikweni ndi Mtengo wa Tamuzi / Nimrodi ndipo ulibe kanthu kochita ndi Yahusha Mesiya kapena Choonadi chopezeka m'Baibulo. Mtengo wa khirisimasi wozengezedwa ndi njoka unali maziko mu Chipembedzo cha ku Babulo.**

Anthu tsopano, ndithudi, alibe njoka yozengeza mtengo wawo, ali ndi nkhata! Koma tisamanamizike ndi kuganiza kuti Yahuwah amavomereza umbuli woterowo m'kulambira kokhazikitsidwa m'chikunja cha ku Babulo… Mitengo ya Khrisimasi ndiyo mitengo ya Ashera kapena mitengo yopatulika yolemekeza "***Ba'ala"*** ndipo zokongoletsazo zikuimira ***maliseche*** a Nimrodi! Khata imaimira ***njoka***, Satana!

Mbiri ya Babulo imasonyeza kuti Nimrodi anadulidwa mzidutswa ndipo ziwalo zake zinatumizidwa ku zigawo zosiyanasiyana za Babulo kuti akachenjeze anthu kuti asapereke ana kwa Moloki. Thupi lake lokhalo lomwe silinapezeke linali chiwalo chokodzera. Semiramis, amayi ake / mkazi wake ndiye adaganiza zokumbukira chiwalo chosowacho ***(chokodzera***) poimika chifaniziro chachikulu cha

chiwalo chokozera cha Nimrod yomwe masiku ano chimatchedwa ***obelisk***. Iwo amakongoletsa mipingo yambiri yachikhristu masiku ano ngati mipanda monga momwe ndanenera poyamba pamutu uno.

***Talamulidwa*** ndi Yahuwah kuti tiwononge izi m'mavesi awa:

***Eksodo 23:24, -Usagwadila milungu yawo…….***

***Eksodo 34:13,Koma mupasule maguwa ansembe awo***

***Deuteronomo 7:5, Koma muzichita nawo motero mukapasule maguwa awo…***

***Deuteronomo 12:3,Nimugumule maguwa ansembe ndikuphwanya zoimilitsa..***

***Yeremiya 43:13, Ndipo adzathyola mizati ya zoimilitsa za kachisi wa dzuwa..***

***Hosea 10:2……adzapasula maguwa awo ansembe ndi zoimilitsa …….***

Komabe, "sitinagwetse malo okwezeka onse" omwe amadzikweza pamwamba pa chidziwitso cha Yahuwah… amawapembedza poyera ngati gawo la Chipembedzo Chachikhristu.

**Mtengo wa Khrisimasi ndiwonso chizindikiro cha satana m'munda wa Edeni, nkhatayo idakulungidwa mozungulira**

**"Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa" ngati njoka yozungulira mtengo wokhala ndi mipira yokongola yoyimira zipatso.**

## CHIYAMBI CHA CHIKRISTU

"Ndizodabwitsa kuganiza kuti zaka zonsezi, zaka mazana ambiri, anthu akhala akutchula Mpulumutsi ndi dzina lolakwika!! Ndikovuta kusiya dzina la Yesu chifukwa lakhazikika kwambiri mwa ife ndipo zambiri zanenedwa. zachitika m'dzina limenelo." Dzina lenilenilo ndi ***Yahusha***. Kumasulira kwenikweni kwa dzinali kumachokera ku **Chihebri**

**Luka 13 34** *"Yerusalemu, Yerusalemu, amene umapha aneneri ndi kuwaponya miyala iwo otumidwa kwa iwe! Ha kawiri kawiri ndinafuna kusonkhanitsa ana ako monga ngati thadzi ndi anapiye ake m'mapiko ake ndipo simunafuna.*

**35** *Onani nyumba yanu yasiyidwa kwa inu ya bwinja ndipo ndinena kwa inu kuti simudzandiona ine kufikira mudzati, wolemekezeka iye amene akudza m'dzina la Yahuwah.*

**3 Chikhristu:chimaphunzitsa kuti Mzimu Woyera alinso "Mulungu" ndi munthu wachitatu wa Utatu ndi wolingana ndi Atate ndi Mwana '**

Palibe paliponse pamene zimenezi zingapezeke m'Malemba. Malemba amatiphunzitsa momveka bwino kuti Mzimu Woyera

ndi mphamvu ndi kufalikira kwa Atate wathu wa Kumwamba Yahuwah ndipo mphamvu imeneyi imaperekedwa kwa Mwana Wake Yahusha amenenso amatipatsa Mzimu Wake.

**Num 11:29** "***Koma mtumiki wanga Kalebu, popeza ali ndi mzimu wina mwa iye, ndipo wanditsatira ndi mtima wonse, ndidzamulowetsa m'dziko limene anapitako, ndipo mbewu yake idzalowamo***.

**2Sam 23:2** ***"Mzimu wa Yahuwah walankhula mwa ine, ndipo mawu ake ali pa lilime langa.***

***Miy 1:23 "Landirani kudzudzula kwanga. Taonani, nditsanulira pa inu mzimu wanga, Ndidziwitsa mau anga kwa inu.***

***Yes.30:1 Tsoka kwa ana opulukira, atero Yahuwah, kupanga uphungu koma wosachokera kwa Ine, ndi kulingalira zolingalira, koma osati za mzimu wanga, kuonjezera uchimo kuuchimo;***

***Yesaya 44:3 Pakuti ndidzathira madzi pa waludzu, ndi mitsinje pa nthaka youma; Ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mbewu yako, ndi madalitso Anga pa mbewu zako***

***Ezekieli 36:27 ndi kuika mzimu wanga mwa inu. Ndipo ndidzakuyendetsani m'malamulo anga, ndi kusunga maweruzo anga, ndi kuwacita.***

***Dan 4:8 Pomalizira pake Danieli, dzina lake ndiye Belitesazara, monga mwa dzina la mulungu wanga, anadza pamaso panga. Mwa iye muli mzimu wa Elohim wopatulika (Yahuwah).***

***Yoweli 2:28 "Ndipo zitatha izi kudzakhala kuti ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa anthu onse. Ndipo ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera, akulu anu adzalota maloto, anyamata anu adzaona masomphenya.***

***Yoh_14:20 "Tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti Ine ndiri mwa Atate wanga, ndi inu mwa Ine, ndi Ine mwa inu.***

*Pali malemba ena ambiri otsimikizira kuti Mzimu ndi Mzimu wa Yahuwah osati mulungu wosiyana wotchedwa Mzimu Woyera***.***

***Mark 1:11 Ndipo mudatuluka mawu m'mwamba, Iwe ndiwe Mwana wanga wokondedwa, mwa Iwe ndikondwera. Mau awa ndi mau a Atate osati mulungu wotchedwa Mzimu Woyera.***

**4 Chikhristu chimaphunzitsa kuti Yesu osati Yahusha ndi Mwana wa Yahuwah.**

Yesu ndi Mesiya wonyenga amene amaphunzitsa zinthu zambiri zosiyana ndi zimene Baibulo limanena.

Chilembo cha **J** sichinakhaleko m'nthawi ya Yahusha , chinangobwera m'Chingelezi zaka 5***00*** zapitazo Yahusha atakwela kale kumwamba choncho zinali zosatheka kuti dzina la Mesiya likhale Yesu(**Jesus mchingerez**).

**Yoh 5:43** "Ndadza Ine m'dzina la Atate wanga, ndipo simundilandira Ine; akadza wina m'dzina lake la iye mwini, ameneyo mudzamulandira.

Izi ndi mwachidziwikire zimene dziko lachita lavomereza Yesu Mesiya wabodza m'malo mwa **Yahusha** Mesiya weniweni. Yesu alibe kalikonse kofanana ndi Yahuwah koma Yahu**sha** ali ndi **Yahu** wofanana ndi Atate Wake. Chidule cha dzina la **Yahuwah** tisaiwale kuti tinafotokoza kale kuti mawu akuti **SHA** amatanthauza **chipulumutso** mu chi Heberi. .choncho dzina loti Yahusha limatanthauza kuti **Yahuwah** ndi **chipulumutso**.

5 **Chikhristu chimaphunzitsa kuti muyenera kubatizidwa m'maina atatu, la Atate, la Mwana, ndi la mzimu woyera**.

Chonde dziwani kuti Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera ndi maudindo osati mayina. Malemba amaphunzitsa kuti pali Dzina **LIMODZI** lokha limene mungapulumutsidwe nalo ndilo Dzina la **Yahusha Mesiya**.

***Machitidwe 4:12 "Ndipo palibe chipulumutso mwa wina aliyense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la***

***kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo.”***

***Machitidwe 19:5 Ndipo pamene adamva ichi, adabatizidwa m'dzina la יהושע (Yahusha) Mesiya.***

***Aroma 6:3 Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tidabatizidwa mwa Yahusha tidabatizidwa mu imfa yake?***

***Agalatiya 3:27 Pakuti nonse amene munabatizidwa mwa Mesiya mudavala Mesiya.***

## 6 Chikhristu chimaphunzitsa kuti Mesiya anapachikidwa pa mtanda

### *Mtengo womwe Mesiya anapachikidwapo*

Akhristu ambiri ali nacho chikhulupiliro chokhazikika m'maganizo mwawo kuti panali mitanda itatu pa Kalvare -wa pakati pomwe Mesiya anapachikidwapo pamene mitanda ina m’mbali mwake panali zigawenga ziwiri. Zingakhale zodabwitsa kuzindikira kuti Baibulo silinena paliponse kuti Mesiya anapachikidwa pa mtanda wa Aroma!

Ndipotu Baibulo limafotokoza momveka bwino kuti Mesiya ndi zigawenga ziwiri zija anapachikidwa pamodzi pamtengo wamoyo, womwe ukukula—kukwaniritsa maulosi

atsatanetsatane komanso zizindikiro zopezeka m'Chipangano Chakale!

**Chizindikiro cha *mtanda* ndi Chizindikiro cha Satana. X/+ ndi chizindikiro cha imfa**.

Zindikirani kuti Baibulo linamasuliridwa m'Chingelezi m'zaka za m'ma 1600 koma linali m'Chigiriki ndi Chilatini.

**Mtanda wofiira ndi chizindikiro cha Azazeli (Satana) momwemonso mtanda wachikhristu.**

. Azazeli ndi mulungu ***wakufa*** wofanana ndi ***dzuwa***.Iye ndi chizindikiro cha ***imfa X*** *ndi* ***chiukitso* +,** chotero kufanana ndi mesiya weniweni YAHUSHA.

Ankadziwika kuti ***Attis wa Phyrgia,***

***Dionysis waku Greece,***

***Tamuzi waku Babulo,***

***Mithra waku Persia***

***ndipo mulungu watsopano Jesus(Yesu) wa Akhristu Xmas***

***ndi Saturnalia kwa Aroma***.

M'nyengo yozizira pa ***22 December*** dzuwa limasowa kwa masiku atatu ndipo limawonekeranso pa ***25 December***. Apa ndipamene mumapeza KHRISTU+MISA KAPENA khrisimasi.

***Kukhulupirira X kapena + ndi kunyazisa ku chiphunzitso chowona cha m'Baibulo.***

Choncho, Yesu akuimilira mngelo wakugwa Azazeli,ankadziwika ndi mayina osiyanasiyana pa nthawi ya ulamuliro wa maufumu osiyanasiyana.

Iye ku ***EGYPT ankatchedwa OSIRIS,***

***PHYRGIAN ankatchedwa ATTIS***

***KUBABULO Ankatchedwa TAMMUZ***

***GIRIK ankatchedwa APOLLO***

***ROMAN ankatchedwa SOL INVINCTUS***

***MEDO PERSIA ankatchedwa MITHRA***

***SUMERIAN ankatchedwa SHAMASH***

***GREEK EGYPTIAN ankatchedwa SERAPIS KHRISTU***

**7 *Chikhristu chimaphunzitsa kuti Yesu Khristu ndi Mpulumutsi wa dziko lapansi***

Kodi zikanatheka bwanji kuti Mesiya wabodza yemwe sanakhalepo ndipo kunalibe padziko lapansi pano kukhala Mesiya weniweni wa m'Baibulo? Pomwe dzina la Yesu langotha zaka 500 zokha.

Kodi mumadziwa kuti Yesu Khristu ndiyedi Wokana Mesiya? Wokana Kristu amatanthauza m'malo monena kuti wokana Yahusha Mesiya., Yesu wonyenga amene amadzinenera kukhala Mesiya koma amachita kusayeruzika.

Yahusha Mesiya ndi Mpulumutsi Weniweni. ***Yohane 5:43 akuti, "Ndadza Ine m'dzina la Atate wanga, ndipo simundilandira Ine;.***

***Yahusha ndi Dzina lenileni la Mpulumutsi wathu ndipo Yesu ndi Azazel wokana Yahusha (Mesiya).***

***Mateyu 1:21 adzabala mwana wamwamuna, nadzamutcha dzina lake Yesu; pakuti iye adzapulumutsa anthu ake.***

Yahusha amatanthauza kuti Yah ndi Chipulumutso. Mawu akuti Yesu alibe tanthauzo ndipo mulibe dzina la Atate koma Yahusha ali ndi dzina la Atate Wake Yah mwa Yahusha.

Yesu ndi mulungu wachikunja. M'dziko lirilonse maina achikunja a Satana ali osiyanasiyana koma lirilonse limaimira atate, amayi ndi mwana kulambira milungu itatu.

Chipembedzo chimene mumachitcha kuti Chikhristu ndi ***Chipembedzo Chachinsinsi cha Babulo*** wakale ndi Aigupto ndipo ndi ***Chinyengo Chachikulu.*** Baibulo ndi malemba a ***Choonadi*** ndipo pali malemba ambiri onena za mesiya wabodza amene adzasokeretsa ambiri. Chinyengo chochuluka m'chipembedzo chimabisika m'chiphiphiritso ndipo chimadziŵika kwa ansembe okha.

## ***8 Chikristu chimaphunzitsa Kulambira Mafano kupyolera mu Zithunzi, Mafano, Mitengo ndi Miyala***

Yahuwah anatiuza kuti tisamapembedze milungu ina iliyonse ndi kugwiritsa ntchito zizindikiro ndi mafano.

***Eksodo 20:4 Usadzipangire iwe wekha fano, kapena chifaniziro cha chilichonse chakumwamba, kapena cha m'dziko lapansi, kapena cha m'madzi a pansi pa dziko lapansi.***

***Levitiko 26:26 Musamadzipangire mafano, kapena fano losema, kapena kuimika fano lamwala m'dziko mwanu kuligwadira. Pakuti Ine ndine Yahuwah Elohimu Wako.***

***Yesaya 45:20 Dzisonkhanitseni nokha, ndi kuyandikira pamodzi, inu opulumuka a amitundu, sadziwa iwo amene aimika Mtengo Wa Chifananizo Chawo, ndi kupemphera kwa Mulungu yemwe sangathe kupulumutsa.***

***Deuteronomo 28:36 Yahuwah adzakutengerani inu ndi mfumu yanu imene mudzaiika kukhala mfumu yanu ku mtundu umene***

***makolo anu sanaudziwe, ndipo kumeneko mudzatumikira Milungu ina.***

***Mtengo*** ndi ***Mwala*** zimkawumbidwa kufanizira Yesu Khristu ndipo anthu kulikonse akupitiriza ndi chonyansa ichi chovomereza miyambo yachilendo ndi yoipa imene inabweretsedwa.

Yesu ameneyu akusonyezedwa pa zithunzi zambiri ali ndi HALO pamutu pake kapena dzuŵa pamutu pake. Yesu akusonyezedwanso atakhomeredwa pa ***Mtanda*** komabe amachita chonyansa ichi chobweletsedwa ndi azungu pa nthawi ya malonda aukapolo ndi utsamunda pa dziko lonse lapansi.Ndipo tsopano mungadabwe koma musaiwale kuti timakhulupirira ***Baibulo*** ndi ***Mesiya Woona***.

Dzina lakuti ***Yesu*** ndi chilatini ***Iesus*** ndi la chiGiriki, IESOUS kutanthauza ***Isis Eos*** (***Horus***) ***Seb Osiris Us . Us*** amapereka ulemu kwa mulungu wachi Greek ***Zeus. Osiris*** ndi mngelo wakugwa ***Azazel***. Uyu ndi ***IHS*** ndipo dzina la ***Yesu*** ndi ***Iesous*** mu Greek ***Ieso/ Iasoiis*** mulungu wachi Greek wa machiritso. Mu Greece wakale mayina achimuna amathera ndi ***sous, sus*** kapena ***us***. Chifukwa chake, ***Ieso*** ndi wamamuna **Iesous.**

***E*** mchi Greek ndi ***H,*** choncho ***IESOUS*** ndi ***IHSOUS*** ndi dzina la ***Yesu*** mu ***Chigiriki*.**

***IHSO, ISIS (HORUS )*** *ndi* **OSIRIS.** Uwu ndiye ***UTATU WA SATANIC.***

***ISIS (HORUS),*** **OSIRIS** ndi **ATHENA ZEUS CHRONOS.**

***Venus, Jupiter*** ndi ***Saturn ku Roma, Semiramis,***

***Tammuz*** ndi ***Nimorod*** ku ***Babulo.***

Kotero, zomwe zikunenedwazi zimatanthauza kuti Yesu mu Chilatini ndi Chigriki **J** asanakhalepo mu Chingerezi Chamakono ndipo akuyimira ***utatu wa satanic***. Chosangalatsa ndichakuti mfumu yachikunja ***Constantine*** anali membala wa gulu lachinsinsi lotchedwa ***SOL INVICTUS*** kapena ***UNCONQUERABLE SUN (dzuwa losagonjetseka). SOL*** ndi Mulungu wachiroma ***Saturn (Satana)***.

Fungulo lake kuti tipeze milungu imeneyi inali ndani kwenikweni ndi mu ***Genesis 6.*** Azazeli anamangidwa unyolo pansi pa piramidi yaikulu ku Igupto wakale. Uyu ndi amene Yesu akufotokozedwa ngati **mulungu wa dzuwa** (***SUNGOD***).

## 9 Chikhristu chimaphunzitsa Chikunja cha Utatu .

Chiphunzitso cha utatu chinalowa m'malo mwa chiphuzitso cha m'malemba kuti pali Elohim mmodzi yekha,***Atate wa kumwamba Yahuwah*.**

Onani Deuteronomo 6:4, Marko 12; 29, Marko 12;32, Yohane 8;54.

Chikhristu chimaphunzitsa milungu itatu yosiyana yonse yofanana mu mphamvu.Baibulo limatiuza kuti pali Elohim mmodzi Atate wathu Yahuwah ndi mwana wake Yahusha ndi mzimu wake amene sali anthu osiyana koma ndi mzimu wa mphanvu wa Yahuwah.

**Pemphero la Chikhulupiriro cha Nicean**.

Yesu Khristu anabadwira ku chikhulupiliro cha ***Nicean*** chomwe chinakhala mawu a chikhulupiriro cha ***chikhristu*** chinalembedwa kulamuliridwa ndi kuyeretsedwa ndi mabishopu 318 ampingo wa ***Katolika(Roman Catholic)*** pamsonkhano wa mchaka cha ***325 A.D.*** Ena amakhulupirira kuti kusinthaku kunachitika ku msonkhano wa Chalcedon ***(Council of Chalcedon) 451 A.D***. Iwo amawerenga…. “Timakhulupirira mwa Mulungu mmodzi, Atate, Wamphamvuyonse wa zinthu zonse zooneka ndi zosaoneka, Mbuye mmodzi Yesu Kristu, Mwana wa Mulungu, wobadwa yekha kwa Atate, amene amachokera ku thupi la Atate, mulungu wochokera kwa Mulungu, kuwala kochokera ku kuwala; Mulungu woona wochokera kwa Mulungu woona, wobadwa wosapangidwa, wogwirizana ndi Atate, amene zinthu

zonse zinakhalapo kudzera mwa iye zakumwamba ndi zapadziko lapansi chifukwa cha ife anthu, ndipo chifukwa cha chipulumutso, iye anatsika nakhala munthu wozunzika. tsiku lachitatu anakwera kumwamba kudzaweruza amoyo ndi akufa ndi mwa mzimu woyera"

## Chiyambi cha Utatu

Akuluakulu adamutsekera ***Arius*** ndikumuopseza kuti amupha kuti atseke pakamwa pake asayankhule kanthu.

Iwo anaika lamulo pa nthawi imene anthu anayamba kuzindikira mabodza ndi chinyengo, ndipo analamula kuti mabuku onse awotchedwe; kuwononga zolembedwa zonse zakale, "***popanda umboni palibe mtsutso***", ndipo chotulukapo chake chinali kusandulika kuchoka pa ***Serapis Christus***, kutanthauza ***Kristu Mpulumuts***i, kupita kwa ***Yesu Kristu*** mwa lamulo la Mfumu ***Constantine mu 325 A.D.***

Yahuwah anati "***Iye ndi Mmodzi***" Deuteronomo 4,6

***Yahuwah ndi Mzimu ndipo Mwana Wake akuwoneka mu thupi. Iwo ali Mmodzi monga Yahusha ali Dzanja Lamanja la Atate.***

Yesu Khristu ndi dzina latsopano lomwe linapangidwa ***zaka 400 zapitazo*** ndi mpingo ***wa Roma Katolika.*** ***Chithunzi cha Yesu ndi mwana wa Papa.*** **Yesu sanabadwire ku Nazarete koma Yahusha ndi amene anabadwira ku Nazarete**.

*Yesu sanayende pa dziko lapansi pano komanso sanafe chifukwa cha machimo anu. Iye ndi Wotsutsa Mesiya "Mpulumutsi" wonyenga amene amaphunzitsa ziphunzitso zosayeruzika, mabodza ndi chinyengo m'Chikristu. Izi zidachitika mwadala kuti akusocheretseni kuti mutaye moyo wanu osatha.*

Kodi muyenera kuchita chiyani tsopano pamene mwadziwa choonadi?

Baibulo limaphunzitsa kuti muyenera kutuluka m'zipembedzo zonse zonyenga kuphatikizapo mipingo yonse ndi zipembedzo zonse chifukwa palibe amene akuphunzitsa choonadi molingana ndi Malemba. Sitingathe kupitiriza kukhala ku Babulo (***mipingo ndi chipembedzo chonyenga)*** ndi kukhala ogwirizana ndi Yahusha Mesiya.

Mzimu Wonyengerera udzakutsogolerani kuti mutaye moyo wanu wosatha. ***Inde ndizoona simudzatchuka chifukwa choyimirira pachoonadi monga kwalembedwa m'Malemba kapena kuchoka ku mpingo wanu koma Yahusha adati ngati anandida nawonso adzadana nanu ndipo ngati adazunza ine adzakuzunzaninso .***

***Kondwerani kuti muli panjira yowongoka ndi yopapatiza; pakuti njira yakumuka nayo ku chiwonongeko ili yotakata***.

*Yahusha ananenanso kuti ngati ukonda atate kapena amayi, mwana wamwamuna kapena wamkazi, mlongo kapena mbale kuposa ine simuli woyenera ine. Ngati mundikana ine Mesiya weniweni Yahusha Mesiya, ndiye Yahusha nayenso adzakukanani inu pamaso pa Atate Wake wakumwamba.* ***Musayike chidaliro chanu mwa munthu, mpingo wanu, kapena m'busa wanu pokhapokha atakuuzani kuchokera m'Malemba okha.***

Zomwe muyenera kuchita ndi kupeza nthawi yophunzira Malemba nokha ndi kuyamba kuphunzira Baibulo pogwiritsa ntchito Malemba onse kuyambira Genesis mpaka Chivumbulutso kuti mumvetse bwino nkhani yomwe mwalandira kapena pa mutu womwe mwapatsidwa.

Yambani kuŵerenga Baibulo pamodzi monga banja ndi kuphunzirira limodzi Baibulo.Pempherani pamodzi monga banja ndi kuuza ena ziphunzitso zosiyanasiyana zimene mukuphunzira m'Baibulo.

Tsiku lina tonse tiyenera kukaonekera pamaso pa Atate wathu wakumwamba kuti tikalandire mphotho yathu molingana ndi momwe tinakhalira ndi moyo wathu. Kodi mwakonzeka kukaonekera pamaso pa Mlengi wa chilengedwe chonse kuti mudzalandire mphotho ya zimene mwakhala mukuchita pa moyo uno?

***Tchimo limafotokozedwa kuti: ndi Kuphwanya Malamulo a Yahuwah ndipo ngati upitiriza kunyalanyaza Lamulo Lake (Torah) Satana adzakhala mbuye wako ndi woyendetsa ukapolo wako ndipo adzalamulira pa moyo wako kukubweretsera masautso osaneneka, umphawi, kudzikonda, kupandukira chifuniro cha Yahuwah ndi imfa yamuyaya***.

Ndi okhawo amene amakonda ***Abba (Atate)*** adzapereka moyo wawo kwa Iye. Yahusha Mpulumutsi wathu Wodabwitsayo analipira dipo la mtengo wapali kwambiri podzipereka Iye monga nsembe yauchimo, kunyamula machimo athu onse pa Iye kuti tithe kumasulidwa ku chilango choopsa cha kuswa malamulo a Yahuwah.

Tiyenera tsiku ndi tsiku kusankha njira yopapatiza yomwe imatsogolera ku moyo wosatha ndipo inde zidzatengera kudzipereka kwanu kusiya mayesero onse adziko lapansi, miyambo ya anthu ndipo zingatanthauzenso kuti muyenera kusiya omwe mumawakonda omwe ali osalolera kusiya moyo uno.

Yahuwah adzakutsogolerani koma choyamba muyenera kukhala woona mtima ndi Abba (Atate) ndikuvomera kuti ndinu wochimwa ndiyeno moona mtima kuulula machimo anu onse ndi kubwera modzichepetsa kwa Iye ndiyeno kupanga chisankho chosinkhasinkha tsiku ndi tsiku ndi kuphunzira

Malemba Ake kuti muthe kukhala ndi mphamvu yakugonjetsa uchimo tsiku ndi tsiku.

Pemphani Abba kuti akutumizireni abwenzi atsopano ndi achibale amene adzakulimbikitsani kukwaniritsa tsogolo lanu langwiro limene Yahuwah ali nalo pa moyo wanu, akukonzekera kukudalitsani ndi kukupindulitsani ***Ngati Mumvera Malamulo Ake (Torah).***

*Kaya mufuna kukhulupirira kapena ayi tonsefe tiyenera kuonekera pamaso pa mpando woweruzira wa Yahusha kuti tidzalandire mphotho molingana ndi zomwe tachita komanso ngati tinavomereza Yahusha Mesiya kukhala Momboli ndi mbuye wathu.*

Kukonda kwathu Yahusha kudzasonyeza zipatso za kumvera lamulo langwiro la Ufulu, Torah. (Malamulo onse a Yahuwah). Chikhulupiriro chenicheni ndi kumvera Yahuwah ndi kukonda kuchita chifuniro Chake chifukwa mukudziwa kuti Yahuwah waika Torah kuti tikhale ndi moyo wodalitsika.

***Muyenera kutuluka mu zipembedzo zonse zopangidwa ndi anthu ndi mipingo ndi kuphunzira Malemba nokha.*** Mipingo yonse yosakaniza choonadi ndi cholakwika chomwe chiri gawo la Babulo kutsatira ziphunzitso za mpingo wa Roma Katolika.

Ife tiyenera kutuluka ndi kupatukana kuti ife tisatenge nawo machimo awo.

Tiyenera ***Kutuluka*** m'zipembedzo zonse kuphatikizapo ***Chikristu*** ngati simukufuna kudzalandira ziweruzo za Yahuwah kwa osamvera, ***Chivumbulutso 18;4*** zimene zili ziphunzitso zopangidwa ndi anthu zosakanikirana ndi miyambo yachikunja ndipo sichiri chikhulupiriro chenicheni cha Yahusha Mesiya.

Tikuyenera kukhala olekanitsidwa (osiyana) ndi dziko lapansi kumvera ndi kutsatira Mpulumutsi wathu Yahusha Mesiya ngati tikufunadi moyo wosatha. Ndi okhawo amene adzapirira mpaka mapeto ndi kumvera Malamulo, malemba ndi maweruzo adzapulumutsidwa.

Chikhristu ndi chipembedzo Chachinsinsi cha Babeloni chomwe chanyenga miyandamiyanda ya okhulupirira owona mtima chifukwa saphunzira Baibulo paokha koma amakhulupirira akulu a chipembedzo monga azibusa, ma bishopu ndi aneneri awo. *Ngati mwasankha kusamvera zimene zinalembedwa m'Malemba, ndiye kuti mulungu wanuyo ndi Satana wosaoneka ngati m'mene aliri "Yesu Khristu."*

***Ngati mukufuna kumva zambiri tipezeni kuno ku Malawi pa websaiti iyi:***

***https: / / malawioutreach.teachery.co/***

***studythecalendar.com  /***

***Kapena pa manambala awa:***

*0888707002/ 0999856135.*